EXAMINATION NUMBER ________________________________

# KAYEMBE ZONE EXAMINATION BOARD

## 2024 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATIONS

## CHICHEWA

(MALIKISI 100)

DATE:____/_______/___________

TIME ALLOWED:_______________

**Dzina lanu:** ________________________________________________

**Dzina la sukulu lanu:** ________________________________________________

**MALANGIZO**

1. Onetsesani kuti pepala ili ndi masamba Osindikizidwa Asanu ndi awiri
2. Pepala ili lili ndi magawo **A, B, C**, ndi **D**
3. Lembani dzina la sukulu lanupa mwamba pa Tsamba lililonse
4. Lembani nambala ya mayeso pa mwamba pa Tsamba ililonse
5. Lembani chimangilizo kapena kalata mu **Gawo A**, Ndipo muyakhe mafunso onse mu **Gawo B, C,** ndi **D**
6. Lembani yakho lanu mu **Gawo A** pa mapepala omwe Ali kumathero kwa ma funso one Gawoli
7. Yakhani mafunso a mu **Gawo B** ndi C m'mipata Yomwe yapelekedwa pansi pa funso lililonse
8. Yakhani mafunso a **Gawo D** pozunguliza lembo lokhoza Pafunso lililonse
9. Muchitebulo chili pamwambachi onetsani funso lililonse Lomwe mwayakha pochonga mubokosi lomwe ilikutsogolo Kwake
10. Perekani kwa okuyang'anirani kulemba mayeso (imvijireta)

Pepala lonseli nthawi ikakwana

| Funso | Chongani zomwe mwayakha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6 | | | |
| 6-10 | | | |
| 11-15 | | | |
| 16-20 | | | |
| 21-35 | | | |
| 26-30 | | | |
| 31-35 | | | |
| 36-40 | | | |
| 41-45 | | | |

## GAWO A ( malikisi 30)

**Yankhani funso limodzi mwa mafunso awiri aperekedwawa. Lembani mawu osachepera 100 ndipo asapitilire 150.**

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu: '**MADZI OSEFUKIRA)'** Mwa zina tsatilani izi polemba:

   **Ndime yoyamba**
   - Dera lomwe kudasefukira madzi
   - Chaka, nthawi ndi mwezi womwe madzi adasefukira

   **Ndime yachiwiri**
   - Zotsatira za madzi osefukira
   - Momwe anthu adathandizidwira

   **Ndime yachitatu**
   - Fotokozani zomwe mungachite pofuna kuthana ndi vuto losefukira kwa madzi

   **KAPENA**

2. Lembani kalata kwa phungu wa nyumba ya malamulo woyimira dera lanu, bokosi 7340,Dowa kuti akupempherení ku boma chipatala m'dera lanu.

   Mwa zina tsatilani izi polemba:

   **Ndime yoyamba**
   - Dzina la dera lomwe chipatala chikufunika
   - Kuchuluka kwa anthu m'dera lanu
   - Kukula kwa chipatala chomwe mukufuna

   **Ndime yachiwiri**
   - Mavuto omwe anthu akukumana nawo
   - Zinthu zomwe anthu a m'dera lanu achitapo

   **Ndime yachitatu**
   - Chipatala chithandiza bwanji m'dera lanu

____________________________________________________________________________
____________________________________________________________________________
____________________________________________________________________________
____________________________________________________________________________
____________________________________________________________________________
____________________________________________________________________________
____________________________________________________________________________
____________________________________________________________________________
____________________________________________________________________________
____________________________________________________________________________
____________________________________________________________________________
____________________________________________________________________________
____________________________________________________________________________
____________________________________________________________________________
____________________________________________________________________________
____________________________________________________________________________
____________________________________________________________________________

**GAWO B (malikisi 20)**

**Kumvetsa nkhani**

3. **Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo.**

Tsiku lina m'mudzi mwa Dima mudabuka nkhwesa pakati pa mbewu ndi ziweto. Mbewu zonse zimadzimva poganizira kuti izo zidali zofunika kuposa ziweto.ziweto nazo zimadzimva kuti ndi zofunkiraso. Mkangano utakula pakati pa mbewu ndi ziweto, mwini munda, a Limani adayitanaitsa msonkhano wachikhadzakhadza wa mbewu ndi ziweto.

Cholinga chamsonkhano chidali choti mbewu ndi ziwetozo zidzathetsane mankhalu polongosola mfundo za ubwino wawo. Nthawi ya msonkhano itakwana, chimanga ndicho chidayamba kuyankhula. Icho chidati;” ife ndife ofunika kuposa wina aliyense pano. Palibe amene angawiringule. Mwachitsanzo ine kundilima n’kosavuta. Ndimafuna kundikonzera mizere yabwino, kundibzala ndi mvula yoyamba mchere usanapite pansi. Ndimafunanso kundithira fetereza okulitsa ndi obereketsa ndiponso kundipalira. Ngati mungasowe fetereza mukhoza kundithira manyowa popeza kupeza n’kosiyana. Mukachita zonsezi mumangondidikira nthawi yochepa kuti ndikhwime. Ine ndimathandiza anthu ndi ziweto m’njira zosiyanasiyana. Ndikasowa pabanja kapena m’dziko pamakhala wemphawempha wadzaoneni. Sindiri ndekha, anzangawa monga a Fodyawa, a Thonje ndi a Mtedza amafuna kuwasamalira. Mwachitsanzo a Fodyawa amafunika kuwasamalira bwino kuchoka ku nazale poti mmera mpoyamba. Amafunanso kuwachotsa sakasi, kuwathyola pa nthawi yake, kuwatchisa mwaluso kuwasankha bwino ndi kuwadinda m’mabelo mopanda chinyengo. Akatero alimi akhoza kukhala ampondamakwacha.

Kenaka m’bwalo mudalowa Ng’ombe m’malo mwa ziweto zonse. Iyo idati,”Zinazi ndi nkhambakamwa chabe. Zenizeni n’zakuti, ine ndi anzangawa ndi amene tili ofunika kwambiri kuposa ena nonsenu. Ine ndimapereka mkaka umene anthu amamwa kuti akhale ndi thanzi. Ndimaperekanso nyama imene amagulitsa ndikupha makwacha ankhaninkhani. Tamva kale kuchokera kwa anzathuwa kuti mbewu zimafuna manyowa kuti zikule ndi kubereka bwino. Manyowawo amachokera kwa ife. Kupanda ife enanu mukadanyentchera.

Popitiriza kuyankhula a Ng’ombe adati,”Nawonso ankhuku ndi aphindu pa moyo wa munthu. Iwo amapereka mazira omwe mlimi angadye ndi kugulitsa. Nawonso a Bulu ndi ine timamuthandiza mlimi pomunyamulira zokolola monga inu mbewu. Nayenso galauza amafuna ife a Ng’ombe kuti mlimi akubzaleni inu Mbewu. Nanga apa mungawiringulenso?”” chitetezonso chili m’manja mwathu. Anzathu monga a Galu amathandiza polondera tonsefe. Iwo amatiteteza ku mbala komanso aGalu amamuteteza mlimi kwa adani ake. A Mphaka nawo amakutetezani inu mbewu ku makoswe omwe angakutheni psiti. Ife sitilira ndalama zambiri kuti atisamalire ngakhale kuti phindu lathu ndi lankhaninkhani. Kungopita nafe kidibi ndi kutisambitsa kapena kutibayitsa jakisoni, mwatitha.

Potsiriza pa msonkhano, a Limani adathokoza kwambiri Chimanga chomwe chidayankhula m’malo mwa mbewu zonse ndi ng’ombe yomwe idayankhula m’malo mwa ziweto zonse. A Limani adayankhula mosapsatira kuti mbewu ndi ziweto ndi zofunika. Mbewu ndi ziweto zimabweretsa chakudya ndi chuma. Chakudyachi ndi monga mondokwa, nsima , mkaka ndi nyama. Mlimi akagulitsa mbewu ndi ziweto, amapeza chuma. Iwo adati Chimanga chikhoza kukhalacha ziweto ndipo ziweto zimathandiza Chimanga kumbali ya manyowa.

A Limani adapitilira kuti mbewu zina zimatha ndalama kuti zifike pozikolola. Adatinso ziweto zimafuna kuzisamalira kwambiri kuti zikhale zopindulitsa. Iwo adauza nyama ndi mbewu zija kuti zonse zidali zofunika.

Potsiriza penipeni a Limani adapepesa kwambiri mbewu ndi ziweto zina chifukwa chosazipatsa mpata woyankhula malinga ndi kuchepa kwa nthawi. Adathokoza mbewu ndi ziweto chifukwa choyankhula momasuka pa msonkhanowo ndipo adafunira mafuno abwino onse adafika pa msonkhanowo. Iwo adapempha kuti mbewu ndi ziweto zizikhala mwa mtendere.

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pansi pa funso lililonse.

a. Kodi nkhaniyi ikuchitikira kuti?
   _______________________________________________________________(1 malikisi)
b. N'chifukwa chiyani mkangano udabuka pakati pa mbewu ndi ziweto?
   _______________________________________________________________(2 malikisi)
c. Perekani chifukwa chimodzi chomwe a Limani adaitanitsira msonkhano?
   _______________________________________________________________(2 malikisi)
d. Fotokozani njira yosamalira fodya.
   _______________________________________________________________(2malikisi)
e. Tchulani ziweto zitatu zomwe zidaimiliridwa ndi ng'ombe.
   _______________________________________________________________
   _______________________________________________________________
   _______________________________________________________________(3malikisi)
f. N'chifukwa chiyani mbewu ndi ziweto zili zofunika?
   _______________________________________________________________
   _______________________________________________________________(2malikisi)
g. Perekani matanthauzo a mawu otsatirawa:
   i) Nkhwesa_____________________________________________________(1 malikisi)
   ii) Mosapsatira__________________________________________________ (1 malikisi)
h. Pezani mawu m'nkhaniyi omwe ali ndi matanthauzo ofanana ndi awa:
   i) Kwinimbira___________________________________________________(1malikisi)
   ii) Zongonena chabe _____________________________________________(1 malikisi)
i. Kodi inu mukadakhala a Limani mukadagamula motani nkhaniyi?
   _______________________________________________________________(2 malikisi)
j. Perekani mutu wa nkhaniyi.
   _______________________________________________________________(2malikisi)

**GAWO C (10 MALIKISI)**

4. Werengani kankhani ndipo muyankhe mafunso otsatirawa:
   " Koma iwe ungakagone kunyumba anzako tili khumakhuma pano", siumfiti umenewu? Ndiye igwa apa mbuzi ziwiri

   **MAFUNSO**

i) Kodi ndi mtundu wanji wa malonje omwe mwawerengawu?
____________________________________________________________(1 malikisi)

ii) Ndani angayankhule malonjewa?
____________________________________________________________(1 malikisi)

iii) Perekani tanthauzo la nsinjiro iyi,” igwa apa mbuzi ziwiri,”
____________________________________________________________(2 malikisi)

iv) Tchulani njira imodzi yotumizira uthenga wa maliro ku mudzi.
____________________________________________________________(1malikisi)

v) Kodi mukamayankhula ndi munthu wamkulu muyenera kutani?
____________________________________________________________(1 malikisi)

**KUPANGA ZIGANIZO**

5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:
   a. gobedegobede
   ____________________________________________________________(1malikisi)
   b. ndi
   ____________________________________________________________(1malikisi)
   c. gule
   ____________________________________________________________(1malikisi)
   d. chipere
   ____________________________________________________________(1 malikisi)
   e. Tsokwe
   ____________________________________________________________(1 malikisi)

**GAWO D (40malikisi)**

**Zungulizani lembo lokhoza (A,B,C kapena D) m’mafunso otsatirawa**

**Mafunso 6 mpaka 10, sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

6. <u>Hi!</u> Mwana uja wagwa.
   A. Mneni C. Mlumikizi
   B. Mfuwu D. Mvekero
7. Amayi akupita <u>ku</u> msika.
   A. Mperekezi C. Muonjezi
   B. Dzina D. Mfuwu
8. Makolo athu <u>amavala</u> nyanda kalero.
   A. Mneni C. Mfotokozi
   B. Mlumikizi D. Mperekezi
9. Mwana <u>wosamva</u> amachititsa manyazi makolo.
   A. Mfotokozi C. Mneni
   B. Muonjezi D. Mlumikizi
10. Mupitebe <u>poti</u> atero.
   A. Mneni C. Muonjezi
   B. Mlumikizi D. Mvekero

**Mafunso 11 mpaka 16.Sankhani magulu a mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi**.

11. Kondwani ali ku <u>munda</u>.
   A. Mu-, Mi- C. Chi-, Zi-
   B. Ka-, Ti- D. U-, Ma-
12. Anthu ambiri amanyadira <u>chinenero</u> chawo.
   A. I-, Zi- C. Ka-, Ti-
   B. Chi-, Zi- D. U-, Ma-
13. Amayi amakonda <u>kusamba.</u>
   A. Ku + tsinde la mneni
   B. Mu-, A-
   C. Ka-, Ti-

D. U-, Ma-

14. Nyumba iyi yamangidwa bwino.
A. I-, Zi- C. U-, Ma-
B. Ka-, Ti- D. Li-, Ma-

15. Tiagalu taluma nkhosa.
A. Mu-, Mi- C. U-, Ma-
B. Li-, Ma- D. Ka-, Ti-

**Mafunso 16 mpaka 20 Sankhani mikuluwiko yofanana matanthauzo ndi yomwe mwapatsidwa m'musiyo.**

16. Apawo ndi mizu ya kachere akumana pansi
A. Zengerezu adalinda kwawukwawu
B. Aonenji adapha mvuwu mmono
C. Kwa eni kulibe mkuwe
D. Atambwali sametana aopa kuchekana

17. Kugona pakati nkuyambirira.
A. Kutola khobwe ndi mmawa
B. Anthu ndi miyala sakukutika
C. Ndapakonda adasiya khonde
D. Likaomba otheratu

18. Mawu akulu akoma akagonera.
A. Mwachaje satafuna
B. Maonekedwe apusitsa
C. Mwini mphale sada chala
D. Mtsinje wa tinkanena udathera msiizi

19. Nzeru zayekha adaviika nsima mmadzi..
A. Safunsa dadya phula
B. Ukapanda mano usamaswa phale
C. Wakwatira mende waleka chitute
D. Zathu salowa mkhola

20. Mutu umodzi susenza denga.
A. Mwachaje satafuna
B. Nguwo yobwereka silimba mthupi
C. Chala chimodzi sichiswa nsabwe
D. Madoli adafera mchenga woyera

**Mafunso 21 mpaka 25 Sankhani mitundu misintho ya aneni omwe ali ndi mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi:**

21. Mlonda wanga wabetsa Katundu
A. Wochititsitsa C. Wochititsa
B. Wochitidwa D. Wochitira

22. Agalu alumitsitsa nyama ija.
A. Wochititsitsa C. Wapadera
B. Wochitira D. Wochitirana

23. Ndani wamanga mbuzi?
A. Wotsutsa C. Wonyazitsa
B. Wochitidwa D. Dzina

24. Mafumu ali bakhalibakhali kwa chalo kufunsa nzeru.
A. Wotsutsa C. Wochitidwa
B. Wobwerezabwereza D. wochitirana

25. Bakha wagundidwa ndi ngolo.
A. Wochitirana
B. Wochitidwa
C. Wochititsitsa
D. Wochitidwa poyera

**Mafunso 26 mpaka 30 Sankhani mvekero woyenera kukhala mu mpata uli m'chiganizo chilichonse m'musimu.**

26. Wafika m'bandakucha kuli___
A. Mbu C. Bi
B. Mbe D. Psu

27. Mbavayo inangoti___kusowa chonena.
A. Yasa C. jenkha
B. Zi D. Phi

28. Atate ali___pakhonde.
A. Zi C. Nji
B. Fwa D. Khuma

29. Pa sukulu panali_____
A. Ndwi C. Mbu
B. Zi D. Phe

30. Mkango unangoti__watulukira
A. Balamanthu C. Mbwe
B. Dera D. Fwanthu

**Mafunso 31 mpaka 35Sankhani mitundu ta nthambi za ziganizo zosaima pazokha zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi:**

31. Zakuti adapita kusukulu ndi zoona.
A. Ya dzina C. Ya mfotokozi

B. Ya muonjezi D. Ya mwininkhani

32. Iwo adachoka titatha kudya.
A. Ya pa mtherankhani
B. Ya muonjezi
C. Ya dzina
D. Ya mfotokozi

33. Abambo avala buluku lomwe agula lero.
A. Ya dzina
B. Ya mfotokozi
C. Ya muonjezi
D. Ya pamtherenkhani

34. Amayi akulima pomwe panali khola la ng'ombe
A. Ya dzina C. Ya mfotokozi
B. Ya muonjezi D. Yoyima pa yokha

35. Yesu adafika kuti tipulumuke.
A. Ya dzina C. Ya mfotokozi
B. Ya muonjezi D. Yoyima pa yokha

**Mafunso 36 mpaka 40 Sankhani ziganizo zomwe zalembedwa m'chichewa chomveka bwino:**

36. A. Wantchito wanga akupanga ulesi.
B. Wantchito wanga ali ndi ulesi
C. Wancthito wanga akuchita ulesi.
D. Wantchito wanga akuonetsa ulesi

37. A. Ndanena kuti musabwerenso
B. ndayankhula kuti Musabwerenso
C. Ndafotokoza kuti musabwerenso
D. Ndati kuti musabwerenso

38. A. Akadzabwera mudzandiuza
B. Adzakabwera mudzandiuza
C. Akadzabwera tidzalinkana
D. Azakabwera mudzandithoka

39. A. Uyenda kuti?
B. ukuvaya kuti?
C. Ukupita kuti?
D. Makava ukulowa kuti?

**MAFUNSO ATHERA APA !!!**

40. A. Namwali uja wakonza lichero lothyoka lija
B. Namwali uja wafotokoza lichero lothyoka lija
C. Namwali uja walongosola lichero lothyoka lija
D. Namwali uja wapanga lichero lothyoka lija

**Mafunso 41 mpaka 45 Sankhani mitundu ya nthawi za aneni ya mawu omwe ali ndi mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

41. Anthu adachita mwayi okumana ku mpira.
A. Nthawi yakale
B. Nthawi yatsopano
C. Nthawi yathayi
D. Nthawi yatsopano yangothayi

42. Mafumu akukumba manda.
A. Nthawi ya mtsogolo
B. Nthawi yatsopano
C. Nthawi yatsopano yapitayi
D. Nthawi yathayi

43. Pakati pa midziyo pali mtsinje waukulu.
A. Nthawi yamtsogolo
B. Nthawi yatsopano
C. Nthawi yakale yopitilira
D. Nthawi yatsopano yopitilira

44. Iye uja amatulukira pa ukwati pokha.
A. Nthawi yatsopano yopitilira
B. Nthawi ya mtsogolo
C. Nthawi yakawirikawiri
D. Nthawi yatsopano

45. Iwo adzagwirizana zoyambitsa timagulu
A. Nthawi ya mtsogolo
B. Nthawi ya tsopano
C. Nthawi yakawirikawiri
D. Nthawi yatsopano yopitilira